NYA_TTB_0937_20161101**_script**

Danieli : 9:1-19

Mutu : Pemphero la Danieli lokhudza Israyeli

Landirani moni wa Kumwamba inu wokondedwa anzanga apaulendo. Lero Ambuye atitsogolere ndi mau apa Luka 15:10, amene akuti, “Chomwecho, ndinena kwa inu, kuli chimwemwe pamaso pa angelo a Mulungu chifukwa cha munthu wochimwa m’modzi amene atembenuka mtima.”

Mupologalamu yatha, tinali kukambirana pa Danieli 8:13-27, momwe timaona kumasulira kwa masomphenya a nkhosa yamphongo ndi tonde. Ndipo lero, pamene tisanthula Danieli 9:1-19, tiona za pemphero la DanielilokhudzaIsrayeli.

Danieli 9

Ichi, ndichapter china chofunika kwambiri m’bukuli komanso m’Baibulo lonse. Tere, mutu waukulu ndiwo wokamba za pemphero la Danieli ndi ulosi wamasabata asanu ndi awiri. Ndiye tikunena motsimikiza kuti, ngati mukhoza kusankhamachapter amene akufotokonza za pemphero, ichi ndichapter chimodzi chofunika kwambiri.Ndime makumi awiri ndi imodzi, a chapter

chonsechi, zikufotokonza za pemphero la Danieli. Ndipo ndime zotsala zisanu ndi imodzi, zikupereka ulosi wofunikira kwambiri wamasabata makumi asanu ndi awiri, momwe tione kutha kwa mphamvu zadziko lapansi, nthawi yomweyo kudza kwa chipulumutso cha Israyeli kudzera mwa Mesiya.

Pemphero la Danieli

Pemphero la Danieli ndilo likuumbamkota moyo wa pemphero wa Danieli. Mukumbukira koyambirirakwa buku lino kuti Danieli ndiye uja anapempha kuti akapempherekayeasanamasulire masomphenya a mfumu Nebukadnezara, ndipo wakhala munthu wa pemphero m'buku lonseli. Pemphero m'chapter chino, likutipatsachitsanzo chamoyowapemphero ndipo likutionetsa nthawi yomwe pemphero lingafunike. Tere, pano ndifuna ndionetse magawo ena ofunika a pemphero:

Kukonzekerakwa cholinga

Kulowa mpemphero sichinthu chongochitamwachangu-changu, kapena mwazagwazatha ayi.Koma kukhala ndi cholinga ndi kudzipereka konse. Tamvani Danieli pa verse 3, adanena kuti,

“ndipo ndinaika nkhope yanga kwa Ambuye Mulungu, kumfunsa Iye m’pemphero ndi mapembedzero, ndi kusala ndi ziguduli ndi mapulusa.” Kutanthauza kuti kwa Danieli pemphero silinangokhala kulankhula ndi timautokometsa, kaya kubwereza-bwereza kwa mau, kaya kukhala ndi lusolosanja mau ayi. Izi, ndizo zinthu zosapindulapakupemphera ndipo Ambuye Yesu mwini pa Mateyu 6:7, adanenetsa kuti, “Ndipo popempheramusabwereze-bwereze chabe iyayi, monga amachita anthu akunja, chifukwa ayesa kuti adzamvedwa ndi kulankhula-lankhula kwawo.”

Kupempheramwaululu

Danieli anapemphera ndi kusala ndi chiguduli ndi mapulusa. Kutsimikiza kuti izi, sizinali kuchitika ndi mtima wofuna kungodzionetsera chabe ayi, koma kuonetsa kudzikhuthula konse kwa mtima wake. Mwachisoni kuti kapempheredwe kotere sikakupezeka masiku ano.

Kupereka chopembedzeramwachindunji

Mupemphero lake Danieli, anangoperekamwachindunjichokhumba chake. Kutanthauza kuti analibe nthawi yoseleula ndi Mulungu

ayi.Kutsimikiza kuti inu ndi ine, timangofunika kupereka chopembedzera chathu mwandunji, osakhotakhota ayi.

Chopemphachikhale chofunika

Tsono Danieli analandira yankho la pemphero lake nthawi yomwe iye anali kupereka chokhumba cha mtima wake, chomwe chinali chofunika, chomwe chinalowam'chifuniro cha Mulungu. Ndikunena mau amenewa chifukwa Danieli atayambakupemphera, mngelo Gabrieli anadza kwa iye kudzapereka kumasulira kwa masomphenya ake. Kutsindika kunena kuti Mulungu amayankhachopempha chofunika pompopompo. Tamvani 1 Yohane 5:14, adanena mau akuti, "Ndipo uku ndi kulimbika mtima kumene tiri nako kwa Iye, kuti ngati tipempha kanthu monga mwa chifuniro chake, atimvera."

Pemphero la m'tseri

Tsono tikaona momwe Danieli anapempherera, sitikuona kuti anapereka pemphero lake pagulu ayi. Iye anapita m'tseri m'nyumba mwake ndi kupempherakwa Mulungu wake. Ambuye Yesu yemwe anali kukonda kupemphera m'tseri monga pemphero

lomwe lili pa Yohane17.Nkhani ikuti payenera kukhala kusiyana pakati pa pemphero la m'tseri ndi lapagulu.Pemphero la m'tseri ndilo limene liyenera kukhala lalitari kusiyana ndi lapagulu.Koma athu ambiri amatenga pemphero la m'tseri kukhala la gulu.Kunena kuti anthu amatalikitsa kwambiri pemphero lapagulu, kukhala ngati la m'tseri.

Pemphero la mphamvu ndi lokhudza

Pano ndiyamba ndi mau akuti pemphero ndilo chidachokhachochamphamvu, chomwe chimalowandikukafikakumpando wachifumu wa Mulungu. Tere taonani zomwe mkulu wina wotchuka pa science, wotchedwa Sir, Isaac Newton, adanena mau akuti, "Ine ndimakhoza kutenga makina ndi kuona nyenyezi zomwe ziri pafupi pano. Koma pamene ndigwada pansi, ndimapyolamlengalenga ndi kukafikakumpando wachifumu wa Mulungu."

Mau onsewa akungofotokonzera kuti pemphero la Danieli linalidilamphamvulochokera mkati mwamtima wake.Ili, ndilo pemphero lomwe likuonetsa kuti kupempherandintchito yobvuta

kwambiri yomwe imafunachipiriro ndi chisauko.Kodi inu mumapemphera motere?

1. Chaka choyamba Dariyo mwana wa Ahaswero, wa mbeu ya Amedi, amene anamlonga mfumu ya Akasidi;

Pano tikuona kuti Dariyo, mwana waAhaswero, wa mbeu ya Amedi, akukhazikitsidwa mfumu ya Babulo, amene analandira mphamvu kuchokera kwa mkulu wa nkhondo, Koresi. Tsono chaka choyamba cha ulamuliro wa Dariyo, m'Medi, ndi 538 B.C. chaka chomwe Amedi ndi Peresiya anali pansi paulamuliro wa Koresi, mkulu wa nkhondo. Ndiye Koresi anatenga ulamuliro wake kwa Dariyo m'chaka cha 536 B.C, nthawi imeneyi mkuti patapita zaka makumi asanu ndi awiri (70 years) zaukapolo wa a Yuda ku Babulo, koma lamulo lakumasulidwa kwawo linali lisanaperekedwe. Ndiye ngakhale zinali chomwechi, Danieli anali atalandira kale bvumbulutso limeneli chifukwa cha chizolowezichokhalamupemphero.

2. Chaka choyamba cha ufumu wake, ine Danieli ndinazindikira mwa mabuku kuti chiwerengo chake cha zaka, chimene mau a Yehova anadzera nacho kwa Yeremiya mneneri, kunena za

makwaniridwe a mapasuko a Yerusalemu, ndizo zaka makumi asanu ndi awiri.

Danieli m'chaka choyamba cha ulamuliro wa Dariyo, anali ndi nkhawa chifukwa chatsogolo la a Yuda omwe anali muukapolo ku Babulo. Pachifukwa chimenechi, Danieli anatsegula mau a Mulungu m'buku la mneneri Yeremiya, amene analosera kuti Israeli adzakhala kuukapolo kwa zaka makumi asanu ndi awiri. Izi, zinachitika m'chaka cha 537 B.C, pamene Danieli anali wokalamba ndithu, kotero kuti anali kudziwa kuti kumasulidwakwa a Yuda kunali pafupi. Kutanthauza kuti anthuwa anali pafupi kupatsidwa mwayi wobwerera kudzikolakwawo.

Tsono tikunenetsa kuti Danieli anadzazidwa ndi mantha maka-maka chifukwa cha Antiokasi, mfumu ya a Syria m'chapter 8.Uyu, ndiye amene Danieli amamuona kuti akhoza kuzunza abale ake.

Wokondedwa anzanga apaulendo, pano ndifuna kunena kuti ngakhale Danieli anali ndi nkhawa, koma analimbikitsidwakupemphera chifukwa cha mau a Mulungu omwe anawerenga.Nkhani ikunena kuti mau a Mulungu ndiwo

amaonetsa chifuniro cha Mulungu pamoyo wanu.Kutsindika kuti kusanthula mau a Mulungu, ndi kutsatira ndi pemphero, ndizo zimathandizira kupeza chifuniro cha Mulungu.Taonani malonjezo a Mulungu omwe Danieli anawerenga pa Yeremiya 25:11, akuti, “Ndipo dziko lonselilidzakhalalabwinja ndi chizizwitso, ndipo mitundu iyi idzatumikira mfumu ya ku Babulo zaka makumi asanu ndi awiri.” Ndiye m’chapter 29:10, ndimomwe adawerenga kuti, “Pakuti Yehova atero, kuti zitapita zaka makumi asanu ndi awiri pa Babulo, ndidzakuyang’anirani inu, ndipo ndidzakuchitirani inu mau anga abwino ndi kubwezera inu kumalo kuno.”

Ndiye ndifuna musunge mumtima mwanu kuti Danieli anali kusanthula ulosi wa Yeremiya wa zaka makumi asanu ndi ziwiri. Tsono pamene mngelo Gabrieli ananena za masaba makumi asanu ndi awiri (V 24), anali kungoonjezera ku zaka makumi asanu ndi ziwiri. Kutanthauza kuti masabata amenewa ndiwo adzakhala chisautso kapena chiyeso cha Israyeli, ufumu wa Mesiya usanakhazikitsidwe.

3. Ndipo ndinaikankhope yanga kwa Ambuye Mulungu, kumfunsa Iye m'pemphero ndi mapembedzero ndi kusala ndi ziguduli ndi mapulusa.
4. Ndipo ndinapempherakwa Yehova Mulungu wanga ndi kubvomereza ndi kuti Ambuye Mulungu wamkuru ndi woopsa, wakuwasungira pangano ndi chifundo iwo akukukondani ndi kusunga malamulo anu.

Tsopano Danieli waika mtima wake pa pemphero. Taonani Danieli wakhazikitsa mtima wake pa pemphero, kotero kuti ndichifukwa chake akunena kuti, "Ndipo ndinaika nkhope yanga kwa Ambuye Mulungu kumfunsa Iye m'pemphero ndi mupembedzero." Apa, ndiye tiyenera kuphunzira kuti nthawi yapemphero ndipo pamene inu ndi ine, tiyenera kuika moyo wathu ndi kudzipereka kwathundu kwa Yehova.

Tsono ine, ndikuchita chidwi ndi momwe Danieli akudziperekerakwa Mulungu. Taonani akudalira kwambiri paubale wake ndi Mulungu. Ichi, ndichifukwa chake akumutchula kuti, "Mulungu wanga."Kutanthauza kuti akupempha Mulunguyo, mwanjira yodabwitsa kwambiri. Ndipo taonani Danieli asanafike

popempha kanthu kalikonse, akuona ukulu ndi kuopsakwa Mulungu. Mwa mau amenewa iye akunena mau akuti, “Ambuye Mulungu Wamkulu ndi woopsa kutanthauza kulemekeza Mulungu kotero kuti sipayenera munthu wina kuchitanayechibwana panthawi ya pemphero.”

Tsono ndapezanso chinthu china chakuti Danieli akudziwa kuti Mulungu amasunga lonjezo lake ndi kuchitira chifundo iwoakumukonda Iye. Kunena kuti Mulungu salonjeza kokha, koma amasunga zomwe walonjezacho.Kutanthauza kuti amachita chinthu chimene walonjezamosakaikira konse.Kutsimikiza kuti Mulungu sasintha, ndiwokhulupirikakomanaowachifundo.Tere ndichifukwa cha chifundo chimenechi, Israyeli anasungika nthawi yonse.Momwemonso inu ndi ine, tikusungika chifukwa cha chisomo ndi chifundo chomwechi. Tamvani Mlaliki 3:22-23, akunenetsa kuti, “Chifukwa cha kusathedwaife ndicho chifundo cha Yehova, pakuti chisoni chake sichileka; chionekachatsopano m’mawa ndi m’mawa; mokhulupirika ndithu.”

5. Tachimwa, tachita mphulupulu, tachita zoipa, tapanduka, kupambuka ndi kusiya maneno anu ndi maweruzo anu;

6. Sitinamvera atumiki anu aneneri, amene ananena m'dzina lanu kwa mafumu athu, akalonga athu, ndi anthu onse a m'dziko.

Danieli akudziika mgulu la anthu ochimwa.Taonani akunena kuti, "Tachimwa," kutsimikiza kuti anali kudzichepetsa pamaso pa Mulungu. Kutanthauza kuti pamene inu mupemphera m'malo mwagulu kapena mpingo simuyenera kunena kuti Mulungu wanga, popeza ili, sipemphero la m'tseri ayi. Pachifukwa chimenechi Danieli akunena kuti iye pamodzi ndi anthu ake, anagalukira Mulungu, kotero kuti anatengedwa ukapolo.

Komanso inu ndi ine, tiyenera kupereka kwa Mulungu zinthu zeni-zenizo zomwe tamchimwira Mulunguyo, osangoti tachimwa, tachimwa osanena chomwe mwachimwa ayi.Ndikunena mau amenewa chifukwa Danieli akutsindika kunena kuti tagalukira Inu.Kutanthauza kuti uchimowo uli m'magulu angapo monga kupalamula, kuchita chodetsa,kupanduka, kusamvera ndi kusamvera atumiki a Mulungu.Inu, muyenera kutchula tchimo leni-leni, monga muja mumamuuzira mwana kuti akagulesopo, machesa ndi sugar, koma osangotiukagule zinthu ayi. Nkhani ikuti

inu muyenera kunenamokhulupirikakwa Mulungu wanu, ngakhale zikhale zochititsa manyazi pamaso pa anthu, koma dziwani kuti Mulungu alibe nyasi kumva machimo anu, popeza akuwadziwa kale.

7. Ambuye, chilungamo ncha Inu, koma kwa ife manyazi a nkhope yathu, monga lero lino; kwa anthu a Yuda ndi kwa okhala m'Yerusalemu ndi kwa a Israyeli onse okhala pafupi ndi okhala kutali, ku maiko onse kumene mudawaingira, chifukwa cha kulakwa kwawo anakulakwirani nako.

Poyamba ndifuna kunena kuti mtima wa munthu umene upereka pemphero kwa Mulungu, uyenera kuzindikira kuti Mulungu ndiye wachilungamo ndi woyera. Ichi, ndichifukwa chake Danieli akubvomera kuti Mulungu anachita mwachilungamopakulanga Israeli. Tere, onani kuti sakumudandaula Mulungu, ndipo akulandira chamanyazi chonse chomwe iwo anachita. Inu ndi ine, tiyenera kumadza pamaso pa Mulungu ndi mtima wotere pamene tikusautsidwa komanso pamene tikupempha chifundo cha Mulungu.Tikunena kuti Mulungu ayenera kutengedwa wolungama m'zinthu zonse zomwe achita. Ife kwathu ndi kudzimvera chifundo,

ichi ndicho anali kunena Danieli pamene amati pakuti takuchimwirani. Ndiye tiyenera kunenetsa kuti Danieli anali kupepesa m'malo mwa mtundu wonse wa Israyeli, kuli konse kumene anali, osati mapfuko awiri wokha a Yuda ayi. Koma sitikutanthauza kuti popeza anthuwa anali omwazika, ndiye kuti ndiwotaika ayipopezadiso la Mulungu lili paiwowa.

Chinthu china chochititsa chidwi ndi chakuti, Danieli akusiyanitsa kulungama kwa Mulungu ndi kuipa kwawo. Taonani akunena kuti Mulungu ndiye wolungama pamene iwo ndiwo woipa, popeza ndiwo amene anamwazika muuchimo wawo. Ndipo Danieli akutsindika kunena kuti popeza iwo ndiwo wochimwa, Mulungu ayenera kulandira ulemu chifukwa cha chilango chake chowayenera a Yudawa. Kutsindika kuti Yehova anachita chilungamo powapereka m'dzanja la mdani wawo.

Wokondedwa anzanga apaulendo, kodi pemphero lanu limaonetsakugonja ndi kudzichepetsa pamaso pa Mulungu?Mwachisoni kuti anthu ambiri amadzamodzilungamitsa pamaso pa Mulungu.Ichi, ndichifukwa china chomwe Mulungu sangamve pemphero lanu.Ndiye ndikoyenera kudza pamaso pa

Mulungu modzichepetsa monga momwe Danieli anafika pamaso pa Mulungu mkupemphera. Tsono ngakhale tidziwe kuti Mulungu sadzataya ana ake kotheratu, koma ngati tidzilungamitsa ndi kupereka zifukwa zoyenerakwa ife eni, tiyenera kuzindikira kuti sadzayankha pemphero lathu.

15. Ndipo tsopano, Ambuye Mulungu wathu, amene munaturutsa anthu anu m'dziko la Aigupto ndi dzanja lamphamvu ndi kudzitengera mbiri monga lero lino, tachimwa, tachita choipa.
16. Ambuye, monga mwa chilungamo chanu chonse, mkwiyo wanu ndi ukari wanu zitembenuketu, zichoke ku mudzi wanu Yerusalemu, phiri lanu lopatulika; pakuti mwa zochimwa zathu ndi mphulupulu za makolo athu, Yerusalemu ndi anthu anu asandukachotonza cha onse otizungulira.
17. Ndipo tsopano Mulungu wathu, mumvere pemphero la mtumikia wanu, ndi mapembedzero ake, nimuwalitse nkhope yanu pa malo anu opatulika amene aliopasuka, chifukwa cha Ambuye.

18. Mulungu wanga, cherani khutu, nimumvere, tsegulani maso anu, nimupenyezopasuka zathu ndi mudzi udachedwawo dzina lanu; pakuti sititulamapembedzero athu pamaso panu, chifukwa cha ntchito zathu zolungama, koma chifukwa cha zifundozanu zachuruka.

Ili, ndipemphero ndi pembedzero la Danieli.Taonani akuyamba kuona momwe Mulungu anaturutsira Israyeli kuchoka ku Aigupto. Ndiye akunena kuti Mulungu anachita ntchito iyi, chifukwa cha chilungamo chake, osati chifukwa cha kulungama kwaanthuwo ayi. Tsono kulungama kwa Mulungu kunaonekera pamene anamva kulira kwawo ndipo anakumbukira pangano lomwe anachita ndi Abraham, Isake, ndi Yakobo (Eks.2:24-25). Kutanthauza kuti chifundo chinadza pa Israeli chifukwa cha kulira kwawo.

Danieli akupempha Mulungu kumasula anthu ake chifukwa cha kulungama kwake. Ndimau awa, tikunenetsa kuti Mulungu ndi wolungama pamene apereka chifundo chake kwa ife popeza Yesu Kristu anapereka kale dipo la machimo athu onse.

19. Ambuye, Imvani; Ambuye, khululukirani; Ambuye, mveraninimuchite; musachedwa, chifukwa cha inu nokha,

Mulungu wanga; pakuti mudzi wanu ndi anthu anu anachedwa dzina lanu.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna titsirize ndi kuona kuti Danieli akupempha Mulungu modzikhuthula kuti amverepempha lawo chifukwa chakulungama kwake, komanso chifukwa lonjezo lake. Anzanga, taonani Danieli sakunena kuti Mulungu amverepempho lawo chifukwa cha kulungama kwaIsraeli ayi. Koma Danieli wakhazikikapakuona dzina ndi ulemerero wa Mulungu basi. Awa, ndiwo maziko pamene tikhoza kuika pemphero lathu.Kodi inu mumapempha Mulungu padzina ndi ulemerero wake, kapena wanu?

Lero tilekeza pano. Ndipo timasanthula Danieli 9:1-19, momwe timaona za pemphero la Danieli lokhudza Israyeli.

Ambuye akudalitseni inu lero. Amen!